NDI MULUNGU UTI?



"Ukhulupirira kuti Mulungu ali mmodzi; uchita bwino..."
— Yakobo 2:19

MAGANIZO AMBIRI

Pali Mulungu mmodzi yekha. Ichi ndi chiphunzitso chomveka bwino cha Baibulo. (Marko 12:29-34) Koma kodi mumadziwa kuti pakati pa Akhristu pali maganizo osiyanasiyana onena za amene Mulungu alidi? Kunena zoona, m'Chikhristu mumalambiridwa milungu yosiyanasiyana, ngakhale kuti mmodzi yekha mwa iyo ndiye Mulungu woona. Ambiri a ife tingakhale

tikulambiradi mulungu wonyenga, ngati maganizo athu onena za Mulungu ndi olakwika. Funso ndi ili: kodi mumalambira Mulungu uti? Kodi mumalambira Mulungu woona wa Baibulo, kapena mumalambira maganizo onyenga onena za Mulungu? Tikumbukire kuti iwo amene alambira Mulungu ayenera kumlambira Iye "mumzimu ndi m'choonadi." (Yohane 4:24)

1. Choyamba, pali chikhulupiriro chakuti Mulungu ndi Utatu. Ichi ndi chikhulupiriro cha Akhristu ambiri. Malinga ndi chiphunzitso ichi, Mulungu ali ndi magawo atatu. Gawo limodzi limatchedwa Atate, gawo lina limatchedwa Mwana, ndipo gawo linanso limatchedwa Mzimu Woyera. Magawo atatu onsewa, kapena anthu atatuwa, amapanga Wokhalapo mmodzi wamkulu. Wokhalapo ameneyu ali ndi mphamvu zonse, amadziwa zonse, ndipo wakhalapo nthawi zonse pamodzi ndi magawo ake atatu, kapena anthu ake atatu.

2. Chachiwiri, pali chikhulupiriro chakuti Mulungu ndi Munthu mmodzi yekha, koma amadzionetsa m'njira zosiyanasiyana pa nthawi zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, m'Chipangano Chakale Iye anali Atate, kenako Iye (munthu yemweyo) anatenga maonekedwe a Mwana pamene Khristu

anali pa dziko lapansi, ndipo pambuyo pake anakhala Mzimu Woyera. Kawirikawiri chikhulupiriro ichi chimatchedwa chiphunzitso cha " Yesu yekha."

3. Chachitatu, pali chikhulupiriro chakuti pali Okhalapo atatu amphamvuzonse amene onse ali ndi ulamuliro ndi mphamvu zofanana ndendende, ndipo kuti onse akhalapo kuyambira muyaya. Onse atatu amanenedwa kuti ndi Mulungu, koma chifukwa chakuti amavomerezana m'zonse zimene amachita, amanenedwa kuti ndi Mulungu mmodzi. Malinga ndi chikhulupiriro ichi, Okhalapo atatuwa (Milungu) anagamula kalekale kwambiri kuti azigwira ntchito zitatu zosiyana. Mmodzi azikhala ngati Atate, wina ngati Mwana, ndipo wina azigwira ntchito ngati Mzimu Woyera.

4. Chachinayi, pali chikhulupiriro chakuti Mulungu ndi Munthu mmodzi yekha, ndipo kuti Munthu ameneyu ndi Atate yekha. Amanena kuti Yesu Khristu analengedwa ndi Mulungu kalekale kwambiri, ndipo anaikidwa pamwamba pa chilengedwe chonse chotsala. Amanena kuti Mzimu Woyera ndi mphamvu ya Mulungu, kapena mphamvu yake yogwira ntchito.

Kodi maganizo onsewa angakhale olondola? Ayi ndithu! Nzoonekeratu kuti anthu onsewa amalambira Milungu yosiyanasiyana! Koma kodi zimenezi zili ndi kanthu? Ndikutanthauza kuti, bola tinena kuti "Mulungu," ndi kuyesetsa kuchita zabwino, kodi zimene timakhulupirira zili ndi kanthu? Inde, zili nako ndithu! Lero padziko lapansi pali chikhulupiriro chofala chakuti zilibe kanthu zimene munthu akhulupirira, bola aitana pa dzina la Mulungu. Awa ndi maganizo onyenga ndi owopsa kwambiri. Baibulo limatiphunzitsa kuti iwo amene sakonda choonadi adzanyengedwa ndipo adzakhulupirira bodza. Chifukwa chokhulupirira bodzali, adzalangidwa (adzatsutsidwa) ndi kuonongedwa. (2 Atesalonika 2:10-12) Yesu mwini ananena kuti: "Ndipo moyo wosatha ndi uwu, kuti akudziweni Inu Mulungu woona yekha, ndi Iye amene munamtuma, Yesu Khristu." (Yohane 17:3) Komabe, tingamdziwe bwanji Mulungu ngati sitidziwa ngakhale amene tikulankhula naye pamene tiitana pa Mulungu? Kodi tikutanthauza:

A. Anthu atatu amene kwenikweni ali Wokhalapo mmodzi?

B. Munthu mmodzi wogwira ntchito m'njira zitatu?

C. Okhalapo atatu amphamvuzonse ochita ntchito zitatu?

D. Munthu mmodzi ndi Mwana wolengedwa?

Tafotokoza maganizo anayi ofala, lililonse losiyana ndi linzake, komabe palibe ngakhale limodzi mwa awa limene limapereka chiphunzitso choona cha m'Baibulo chonena za Mulungu.

MULUNGU WOONA

Kodi mawu oti "Mulungu" amatanthauza chiyani? Kawirikawiri mawuwa amanena za chinthu chilichonse chimene chimaonedwa ngati chapamwamba, kapena chimene chimalambiridwa. Koma Baibulo limaphunzitsa kuti pali Mulungu mmodzi yekha woona, ndipo kuti Mulungu ameneyu ndiye Wokhalapo wamkulu koposa m'chilengedwe chonse. Zinthu zonse zichokera kwa Iye, mphamvu zonse ndi zake, ndipo Iye ndiye wolamulira zonse. Kodi Munthu ameneyu ndani? Malinga ndi Baibulo, Munthu ameneyu ndi Mulungu Atate yekha.

- Mulungu mmodzi ndi Atate wa onse, amene ali pamwamba pa onse. (Aefeso 4:6)
- Koma kwa ife kuli Mulungu mmodzi, Atate, amene zinthu zonse zichokera kwa Iye. (1 Akorinto 8:6)

Mulungu wamkulu ameneyu, Atate, Ambuye Mulungu Wamphamvuyonse, anali ndi Mwana. Kalekale m'masiku a muyaya, Mulungu ameneyu anabala, kapena anatulutsa, Mwana kuchokera mwa Iye mwini. Mwana ameneyu sanalengedwe; Iye anabadwa. Kulenga ndiko kupanga chinthu kuchokera ku zinthu zakunja kwa Mlengi, kapena kuchokera popanda kanthu; koma kubadwa, m'nkhani ino, ndiko kutulutsidwa kuchokera mwa Atate mwini.

MWANA WA MULUNGU

Mwana wa Mulungu anali wofanana ndendende ndi Atate wake. Iye anabadwa m'chifaniziro chake chenicheni, ali ndi chikhalidwe chomwecho choyera ndi chopatulika. Mulungu anapatsa Mwana ameneyu mphamvu zake zonse ndi ulamuliro wake wonse, ndipo mwa Mwana ameneyu, Yesu Khristu, Mulungu analenga chinthu chilichonse m'chilengedwe chonse. (Onani Aefeso 3:9; Ahebri 1:2.) Buku la Miyambo limatiuza za kubadwa kwa Mwana

wa Mulungu, ndi za ubale umene Iye anakondwera nawo ndi Mulungu m'masiku dziko lapansi lisanalengedwe. Ngakhale kuti Iye akutchedwa "nzeru," komabe nzoonekeratu kuti ndimeyi ikunena za Mwana wa Mulungu. Tiyenera kuzindikira kuti mu 1 Akorinto 1:24 Khristu akutchedwa "nzeru ya Mulungu."

> *Yehova anali nane poyamba njira yake, asanalenge zakale. Anandiika chikhalire, kuyambira pachiyambi, dziko lapansi lisanakhaleko. Pamene panalibe zozama ndinabadwa; ... Mapiri asanakhazikike, zitunda zisanakhale, ndinabadwa: ... Pomanga Iye kumwamba ndinali pomwepo ... polemba Iye maziko a dziko lapansi: pamenepo ndinali pa mbali pake, ngati mmisiri; ndipo ndinali wokondweretsa wake tsiku ndi tsiku, ndi kusekera pamaso pake nthawi zonse; ndi kusekera m'dziko lake lokhalamo anthu; ndipo zondikondweretsa zinali ndi ana a anthu.*
>
> — Miyambo 8:22-25, 27, 29-31

Yesu mwini akutiuza kuti Iye anali Mwana wobadwa wa Mulungu. Iye akuti, "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha." (Yohane 3:16)

Mwana wa Mulungu ameneyu, Yesu Khristu, ndiye amene Mulungu anamtuma kudziko lapansi kuti afere machimo a anthu. Ndiye amene anali m'maonekedwe a Mulungu (Afilipi 2:6), komabe anaika pambali ulemerero umene anali nawo pamodzi ndi Atate wake, nadzichepetsa, kuti akhale munthu wosauka ndi womvetsa chisoni. Iye analola kunyozedwa, kumenyedwa, kuchitidwa chipongwe, kutukwanidwa, ndi kupachikidwa mwankhanza, ndipo anapirira kulekanitsidwa ndi Atate wake wokondedwa, kuti ife ochimwa tikhale ndi moyo. Iye amene anapereka moyo wake anali Mwana wa Mulungu. Iye anali ndi chikhalidwe chenicheni cha Mulungu, chifukwa anabadwa mwa Mulungu. Ichi ndi chodabwitsa chachikulu tikaganizira kuti Mulungu anapereka Mwana wake wokondedwa wa Iye yekha; Iye amene anachokera m'chifuwa ndi mumtima mwenimweni mwa Atate. (Yohane 1:18)

ZOONADI ZIWIRI ZOFUNIKA

Pali zoonadi ziwiri zimene zili maunyolo ofunika kwambiri mu dongosolo la chipulumutso. Izi ndi zoonadi zimene tiyenera kuzikhulupirira ngati tikufuna kupulumutsidwa.

1. Choonadi choyamba ndicho chikondi chodabwitsa cha Mulungu pa banja la anthu. Chikondi ichi chinali chachikulu kwambiri, kotero kuti Mulungu anapereka Mwana wake kuti akhale munthu ndi kufera anthu.

2. Choonadi chachiwiri chachikulu ndi chakuti Khristu anafa kuti alipire mtengo wa machimo athu. Iye sanangonamizira kufa, koma anafadi, mwa choonadi chenicheni.

Tsopano ziphunzitso za Chikhristu zimanena kuti Yesu Khristu sanali kwenikweni Mwana wa Mulungu m'njira yeniyeni!! Ena amati Iye sanabadwe mwa Mulungu, koma kuti Iye anali Mulungu wamuyaya mwini. Ena amati Iye analengedwadi ndi Mulungu!! Maganizo onyengawa amatsutsana ndi zoonadi ziwiri zofunika zimene tangotchulazi.

UMBONI WA CHIKONDI CHA MULUNGU

Mulungu anapereka Mwana wake ku zowawa ndi imfa chifukwa anakonda inu ndi ine. Zinapweteka mtima wa Mulungu kuona Mwana wake mwini akuzunzika ndi kufa, koma Iye anakukondani "kotero" kuti anapereka chimene chinali chamtengo wapatali koposa kwa Iye; Mwana wake mmodzi yekha, kuti inu mukhale ndi moyo!

Ndithudi tingaone kuti Mulungu wamkulu ameneyu ali ndi chikondi chachikulu kwambiri pa ife.

Kodi nchifukwa chiyani Akhristu tsopano akuphunzitsa kuti Yesu sanabadwedi mwa Mulungu, koma kuti Iye nthawi zonse anali gawo la Mulungu wa "atatu mwa mmodzi," m'mene onse atatu anali ofanana mu mphamvu ndi ulamuliro? Kodi Baibulo linanama pamene limati "Mulungu anatuma Mwana wake kudziko lapansi"? (1 Yohane 4:9)

Ena amati Mulungu analenga Yesu, kenako anampereka kuti apachikidwe. Kodi zimenezi zikuonetsa chikondi cha Mulungu? Ayi ndithu. Maganizo a Satana awa amapangitsa kuoneka ngati Mulungu kwenikweni ndi munthu wadyera amene anapereka nsembe cholengedwa chake, koma Iye mwini sanapereke nsembe iliyonse. Pokhapokha tikazindikira kuti Yesu anali, ndipo alidi, Mwana woona, wobadwa wa Mulungu; wokondedwa wake, wotuluka mwa Iye mwini, m'pamene tingamvetse kuti Mulungu ayenera kutikonda kwambiri motani. Timamvetsa zimenezi chifukwa Iye anali wofunitsitsa kupereka mphatso yotere; kuzunzika pamodzi ndi Mwana wake pamene anafa mu

ululu woopsa wa thupi, wa maganizo ndi wa mzimu. Iye anachita zimenezi kuti anthu ochimwa ndi omvetsa chisoni akhale ndi mwayi wokhala mu chimwemwe chosatha.

Mdani wa Mulungu ndi wa choonadi chake, mdierekezi, wayesetsa kwambiri kuwononga choonadi chachikulu koposa m'chilengedwe chonse; choonadi cha chikondi chodabwitsa cha Mulungu pa mtundu wa anthu ochimwa. Kodi tingachizindikire bwanji chikondi chimenecho? Timachiona chikondi chimenecho pokhapokha tikamvetsa kuti anali Mwana wake mwini, wokondedwa wa m'chifuwa chake, Mwana wake wobadwa yekha, amene Mulungu anapereka chifukwa cha ife. Koma Satana wanyenga mipingo ya Chikhristu. Iye watsogolera anthu amene ayenera kuteteza choonadi ichi kuti achiwononge, ndipo lero Akhristu ambiri amaphunzitsa kuti ngakhale Yesu amatchedwa Mwana wa Mulungu, Iye sali kwenikweni Mwana wa Mulungu m'njira yeniyeni.

Kuyeneranso kukhala koonekeratu kuti ngati Yesu sanali Mwana wa Mulungu, koma Mulungu mwini, ndiye kuti sikukanakhala koona kuti Iye anafera machimo athu,

chifukwa Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu sangafe. (1 Timoteo 6:16)

KUMENE ZINAYAMBIRA

Zaka pafupifupi 1700 zapitazo, m'chaka cha 325 pambuyo pa Khristu, akatswiri akuluakulu a maphunziro a Mulungu a Mpingo wa Katolika anasonkhana pamodzi pamalo otchedwa Nikaya kuti akambirane ngati Yesu analidi Mwana wa Mulungu kapena ayi. Ena a iwo, motsogozedwa ndi munthu wotchedwa Arius, ananena kuti Iye analidi Mwana wa Mulungu, osati cholengedwa, koma wobadwa mwa Atate.

Gulu lina, lotsogozedwa ndi munthu wotchedwa Athanasius, linagamula kuti Iye sanabadwedi mwa Mulungu m'njira yeniyeni, koma kuti Yesu analidi gawo la Mulungu. Athanasius anagamula kuti Mulungu analidi Wokhalapo mmodzi, kapena "chinthu" chimodzi, chokhala ndi magawo atatu otchedwa Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Lero, Akhristu ambiri akugwirabe chikhulupiriro ichi mu mtundu wina uliwonse. Pochita zimenezi, onsewa akukana choonadi chakuti Yesu analidi Mwana woona, wobadwa wa Mulungu! Msonkhano uwu wa ku Nikaya ndi kumene maganizo onyengawa anayambira, ndipo

kwa zaka 1600 zapitazi akhazikika m'maganizo a Akhristu ambiri.

Funso ndi ili: kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu?

Mwalandira kapepala aka chifukwa Mulungu afuna kuti mudziwe kuti amakukondani kwambiri. Afuna kuti mudziwe kuti chikondi chake pa inu nchachikulu kwambiri, kotero kuti "sanamane Mwana wake wa Iye yekha, koma anampereka chifukwa cha ife tonse..." (Aroma 8:32)

Ngati mukhulupirira ichi, mokhulupiriradi, chikondi cha Mulungu chidzasintha moyo wanu. Mudzakhala ndi chiyanjano ndi Mulungu woona ndi Mwana wake (1 Yohane 1:3), ndipo mudzapatsidwa malo mu ufumu wa Mulungu.